KUKONDWERERA CHIYERO

MMENE MUNGAYAMBIRE GULU LALING'ONO

MPINGO WA NAZARENE CHIGAWO CHA AFRICA

www.africanazarene.org

Kodi Gulu laling'ono ndi Chiyani

Gulu laling'ono mumpingo likutanthauza gulu la anthu oyambira (atatu mpaka khumi ndi awiri) amene amasonkhana kawirikawiri ndi cholinga chomudziwa Ambuye Yesu komanso kumutsatira nthawi zonse pamoyo wawo. Cholinga chagululo chimakhazikitsa cholinga chagulu, umembala wake komanso zilinganizo kapena zochita zake.

Kodi Cholinga Chake Ndi Chiyani

Mipingo imasonkhana m'magulu aang'ono ndi cholinga chokhala ndi nthawi yolingalira ndi kuphunzira mawu a Mulungu, komanso kulimbikitsa maubale mwapangano ndi Mulungu ndi mpingo komanso anthu paokhapaokha ndi cholinga chokondwerera chiyero.

Cholinga chenicheni cha 'Kukondwerera Chiyero' m'magulu aang'ono ndikupitiliza kukhala muchiyanjano cha chiyero pakati pa Akhristu, kuyeretsedwa kwathunthu, kulimbikitsa kulapa ndi kutembenuka mtima kwa ochimwa, kumangika muchiyero komanso kufuna kuti kudzichepetsa komanso mphamvu ya uzimu ionekere kwa Akhristu ampingo wa Chipangano Chatsopano (Buku La Malamulo ndi Mayendetsedwe A Mpingo Wa Nazarene *2009-2013*, ¶25).

Kodi Mungayambe Bwanji Gulu Laling'ono

- Dziwani mtundu wagulu limene mukufuna kuyambitsa komanso kudziwa cholinga chake
  - Kodi ndi gulu lakupemphera ndi kusalakudya, Kuphunzira mawu a Mulungu, Kapena gulu lolimbikitsa ma ubale komanso mapangano?
  - Kodi amene adzakhale mamembala anu ndi ndani? Kodi aliyense angathe kukhala membala wagululo kapena anthu ochita zofanana kapena azaka ziti?

Kuchuluka kapena kuchepa kwa anthu amene ali mugululo kungathe kulimbikitsa kuti anthu ayankhule momasuka kapena ayi komanso kudziwana kapena ayi.

- Kodi gululo ligwire ntchito yake kwa nthawi yotani? Panthawi yamaphunziro akuchitapo kanthu kapena kupitirira apo (miyezi itatu ndi theka, miyezi isanu kapena kupyolera apo)
- Kodi phunziro limodzi likhale ndi nthawi yotani? Mwina ingathe kuyambira pa ola mpaka ola ndi theka

- Khalani ndi ndondomeko ya magulu ang'onoang'ono amene mukufuna kuyambitsa
  - Zindikirani za magulu aang'ono amene mulinawo kale mumpingo wanu
  - Unikani zadera lanu, kuthekera kwake, komanso kuchita bwino kwa izi pokwaniritsa zolinga za gulu lanu
  - Muganizire ichi ngati mwayi wolunjikanso, kuyambanso kapena kulimbikitsa magulu anu
  - Molingana ndi kukula kapena kuchepa kwa mpingo wanu komanso kupezeka kwa atsogoleri odzipereka, muyenera kukhala ndi magulu oyambira pa mamembala atatu kunka mtsogolomo
- Mukhale ndi zipangizo zoyenera kuphatikizapo mabuku kapenanso Buku Lopatulika ndi zolembedwa kuchokera ku Chigawo cha Afilika champingo wathu kuti mukwanilitse zolinga zimene mwaika
  - Onetsetsani kuti Abusa anu pampingo avomereze zipangizo zimene mukufuna kugwiritsa ntchito pagulu lanu laling'ono

Mupeze anthu ena pa mpingopo kuti athandizire ndi atsogoleri omwe. Iwo amene akuthandizira ntchito zosiyanasiyana sayenera kukhala atsogoleri pa gulupo kuti asatanganidwe kwambiri.

- Musankhe malo okumaniranako komanso malowo akonzedwa bwino pokonzekera msonkhanowo
- Mulengeze ndikuitana Anthu kumisonkhanoyi. Munene moyenera za cholinga komanso zochitika kumisonkhano yamagulu

aang'ono komanso nthawi, malo ndi atsogoleri Ake komanso mamembala amaguluwo.

- Zoyenereza pa umembala wagulu nazi:
  - Kukhumba komanso kukhala ndi njala ya chiyero
  - Kudzipereka posonkhana pa nthawi zoikika komanso pafupipafupi
  - Kudzipereka pokhazikitsa kudalirana komanso kusunga zinsinsi zagululo
  - Kukhala ndi mtima wozindikira komanso kuyamikira kudzipereka kwawo pagulu laling'ono monga:
    - Mwayi ophunzira kukhala ngati Yesu Khristu
    - Gulu limene lilimbikitse ubale komanso kudalirana kuti akhale ngati Yesu
    - Kumasuka ndi kulikonda gulu

- Choyenereza gulu chimodzi chadziwika, kukhala ndi pangano loyenera komanso kudalirana wina ndi mzake pagulu kuyenera kulimbikitsidwa ndi membala aliyense aliyense.

Ntchito Ya Mtsogoleri wa Gulu Laling'ono

- Kutsogolera misonkhano komanso kuonetsetsa kuti gulu likukhazikika pa zolinga zake polunjika pazokambirana ndi zochitika zake. Izi ndi monga:
  - Kukonzekera nthawi isadafike
  - Kulunjika pazokambirana kapena zochitika za gulu komanso kutsiliza zochitika pa nthawi yake kuti zisasokoneze mwini malo komanso mamembala kuti asakafike mochedwa kunyumba zawo
- Kupeza ndi kulimbikitsa luso lakayendetsedwe ka gulu monga:
  - Kuonetsa chikondi. Onetsani chikondi chosasinthika komanso kulandira membala aliyense monga Yesu adachitira
  - Kumvera komanso kuyankhapo ndi chifundo. Tsimikizirani aliyense amene akuyankhula kuti zimene akunena ndi zofunika komanso ndi zomveka
  - Pemphani thandizo lawo. Vomerani pamene yankho silikudziwika ndipo membala aliyense wagulu akhale ndi mpata wopereka mfundo zake

- Mulimbikitse mafunso amene angathandize kuti mamembala amasuke kukambirana ndi kuyankha mafunso ena. Mafunsowa angathe kufunsidwa motere Kodi ndi ndani, Kodi ndi Chiyani, kodi ndi nthawi yanji, Kodi ndikuti komanso Kodi motani. Muyembekezere mayankho. Musachititse manyazi kapena kuseka pamene wina sakudziwa yankho

- Kupeza luso lakulimbana ndi zovuta pokhudzana ndikusiyana kwa mamembala pachikhalidwe, kusalunjika pa mutu wazokambirana, miseche imene yapemphedwa ngati pemphero lapadera ndi zina zoterezo. Muthane ndi zovuta mwanzeru
- Kudalira Mulungu polimbikitsa ndikuthandiza gulu laling'ono kufikira zolinga zake. Mukhale ndi mapulani koma mudalire Mulungu kuti atsogolere pazochita zonse
- Zoyenera Kuchita Pa gulu laling'ono
- Kupemphera ndi Kusala Kudya
  - *Mphindi khumi ndi zisanu (15 minutes*) imbani nyimbo komanso kuperekera umboni pa mapemphero amene ayankhidwa kale. Muziunikira pa mapemphero ngati akhala akuyankhidwa ndi amene sadayankhidwe
  - *Mphindi khumi ndi zisanu (15minutes* :) Werengani ndime kapena vesi ya m'Buku Lopatulika koma musalalikire kapena kuphunzitsa
- *Mphindi makumi atatu (30 minutes) kwanthawi yochepa, gawanani zopempherera malingana ndi ndondomeko yapemphero, cholinga chagulu komanso ndikuyanjana mpemphero.*
- Kuphunzira Mawu a Mulungu
  - *Mphindi khumi ndi zisanu (15 minutes*) Mukhale ndi nthawi yachiyanjano kwa nthawi yochepa kenako mukhale ndi nyimbo yotsekulira zonse komanso pemphero
  - *Mphindi makumi atatu (30 minutes*) werengani vesi yaphunziro ndipo mukhale ndi nthawi yamafunso pokuthandiza ndikukwaniritsa cholinga chaphunziro lanu. Fufuzani kuti muzindikire: Kodi vesiyo ikutanthauzanji kodi ingagwiritsidwe ntchito motani panopa. Mamembala m'magulu ang'onoang'ono apereke maganizo awo

- *Mphindi khumi ndi zisanu (15 minutes*) Mukhale ndi nthawi yogawana zopempherera komanso kuuzana zosowa za aliyense pokhudzana ndi phunziro ndipo mukhale ndi nthawi yakupemphera. Muzikhala ndi nthawi yofufuza mapemphero amene ayankhidwa kapena ayi

➢ Pangano komanso kuuzana (ubale pakati pa Mulungu ndi Mpingo)

Gulu laling'ono lingathe kuyambikanso pamene pali kukhumba kolimba kwa kuyenda ndi Mulungu koposa

- Imbani nyimbo yayifupi ndikutsekula zonse ndi pemphero. Mungathe kusankha wina mugululo kuti apemphere kapena kutsogolera nyimbo
- Mutsatire mafunso okhudza ma ubale amene tagwirizana monga;
  - Kodi moyo wanu uli bwanji? Ena amati munthu wamkati ali bwanji?
  - Kodi mukuchitaponji pothandizira kuti mukule m'moyo wanu wa uzimu?
  - Kodi mudali ndi mwayi otani musabatayi potumikira ena ndipo mudatumikira motani?
  - Kodi mudakumana ndi mayesero otani ndipo mudawagonjetsa motani?

Kwa nthawi yochepa mugawane ndi kuuzana zosowa kuzipempherera kenako mupempherere wina ndi mzake. Nthawi zonse muyenera kuunikiranso mapemphero anu kuti muone ngati ayankhidwa kapena ayi.

Mfundozi zakonzedwa ndi Mbusa Mayi Daphne Mathebula amene ndi woyang'anira maphunziro a Sande Sukulu ndi kukula muuzimu ku chigawo cha Mpingo wa Nazarene muno mu Afilika ndipo amakhala kudziko la South Africa.